## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NYENGO MSABATAYI**


**KUYAMBIRA PA 18 FEBRUARY MPAKA 24 MARCH, 2024**

### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyambira mawa pa 18 mpaka lamulungu pa 24 March 2024, tiyembekezere nyengo ya mphepo ndi ya mitambo komanso ya mvula yamabingu yomwe pena idzibwera yamphamvu m'madera akumpoto ndi madera ena am'chigawo chapakati pomwe m'madera akumwera mvula idzigwa yapatalipatali. Izi zili chonchi kamba ka mphepo zochokera kumvuma zomwe pena zikhale zikukumana ndi mphepo zochokera kumwera chakumvuma. Mphepo ya Mwera ikhala ikuomba nthawi zina m'sabatayi.

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

M'madera ambiri kunagwa mvula yomwe inali yamphamvu m'madera akumpoto komanso kum'mwera. Mlingo okwera kwambiri unali wa **170.3mm** ochokera kwa Khanda ku Zomba ndi wa **135.2mm** kuchokera ku Zalewa Agriculture. Kunatentha kwambiri dziko lonse poyerekeza ndi katenthedwe ka mwezi wa March mzaka zambuyomu komwe madigiri anaposa ndi mlingo wapakati pa **3 – 5.4°Celsius**. Ku Mimosa ku Mulanje ndikomwe kunatentha kwambiri kuposa mlingo okhazikika (average) ndi madigiri oposa **5.4 Celsius**.




*Mapu 1: Mvula yoposa mlingo wa 40mm. Mapu 2: katenthedwe kuyambira pa 11 mpaka pa 17 March 2024.*

### MALANGIZO M'SABATALI

- Tipewe kuwoloka kapena kuyendetsa galimoto m'madzi osefukira kapena pomwe akuthamanga kwambiri.


***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*


**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 17 March, 2024**